

**Nkhani Yodabwitsa ya Debora**  
**Kuchokera**  
**ku HIV Kufika kwa Khristu**



---

**HEALED IN VICTORY MINISTRY INTERNATIONAL**

Director: KoHsin Illingworth

Email: [kohsinillingworth@hotmail.com](mailto:kohsinillingworth@hotmail.com)

Web: [www.healedinvictory.org](http://www.healedinvictory.org)

Pastor Chikuta  
+265 999 627 114

Dzina langa ndine KoHsin, ndidabadwira ku Taipei. Ndidakuzidwa ndi makolo wodabwitsa kwambiri amene sanali osauka kapena olemera, bambo anga adabadwira ku Kaoshung, pamene amayi anga adabadwira Kumpoto kwa Taiwan. Zachisoni, amayi anga adamwalira patapita zaka ziwiri akulimbana ndi nthenda ya khansa ya mmapapo.

Makolo anga onse awiri adagwira ntchito molimbika kwambiri ku banki ya First Commercial. Adapereka maphunziro abwino kwa ine ndipo kufikira lero ndine wothokoza kuchokera pansu pa mtima pa chilichonse adandichitira.

Ndinali mwana wamantha kwambiri. Silinali bvuto losowa ndalama, koma ndimkangomva kusowekera chikondi ngakhale kuti makolo anga adayesetsa kundipatsa zosowa zakuthupi. Tsiku lina, ndili ndi zaka 15, ndimkapita kunyumba kuchokera ku sukulu kudutsa pa tchalitchi pamene ndidamva kuyimba kokoma kopembedza, choncho ndidalowa mkati ndikukhala pansu kumbuyo kumamvera kwaya imkayimbayo. Ichi chinali chiyambi changa chomapita ku tchalitchi.

Sindimkadziwa chilichonse chokhudza Yesu Kristu. Ndimkadziwa kuti ndimkakonda mayimbidwe omwe ndidakopeka nawo. Ndimkayimbanso piano choncho ndidayamba kumabwera ku chiyanjano chawo ndi ku gulu losanthula mawu.

Ndili ndi zaka 18, ndidawafotokozera makolo anga kuti ndikufuna kubatizidwa moyenerera kuti ndikhale Mkristu. Izi ndizomwedi ndidachita. Makolo anga sadabwere pa ubatizo wangawo koma ndikudziwa ndithu kuti amkandikonda kwambiri ndipo adamvomereza chisankho changa. Mwachisoni, pambuyo pake ndidalephera mayeso olowera ku yunivesite ofanana ndi mayeso a mulingo wa A ku UK. Zotsatira zake bambo anga adandifunsa kuti ndichita chiyani ndipo ndidapemphera, ndikuthokoza Mulungu popeza Abusa anga ku tchalitchi kuja adandibvomereza kukaphunzira ku yunivesite yatsopano ya Chikristu yotchedwa Koleji ya Khristu. Choncho ndidalemba mayeso ndikuloledwa mwachipambano kukaphunzira za Kulumikizana zomwe ndidamaliza nchaka cha 2002 ndikukhoza kowirikiza pa za Kulumizana ndi Chingerezi.

Mu zaka zanga zinayi zamaphunziro abwino ku Koleji ya Krsitu ndidaphunzira Baibulo ndipo aphunzitsi anga anali atumwi a ku Amerika. Anali maziko olimba kwambiri a chikhulupiriro changa cha Chikristu. Tsopano ndikaona

m'mbuyo ndimayamikira kwambiri chifukwa cha zaka zinayi zomwe Mulungu adandithandiza kuphunzira pa malo abwino ndi kukula mwamphamvu mu chikhulupiliro changa cha Chikristu.

Nditamaliza maphunziro ku Koleji, ndidaganiza zokaphunzira ku maiko a kunja, kufuna kupeza maphunziro a ukachenjede ndipo zidanditengera zaka ziwiri. Ndidapempha Mulungu ndipo ndidaloledwa pa univesite ya Nottingham Trent ku UK kukaphunzira zokhudza utolankhani wa dziko lonse lapansi. Loto langa nditafika zaka 24 linali loti tsiku lina ndidzagwire ntchito ngati mtolankhani wa BBC. Komabe, mu zaka zanga ziwiri zophunzira ku UK, ndidamufulatira kwathunthu Mulungu. Ndidamusiyiratu. Ndikudziwa ndinali Mkristu koma ndidayamba kumwa mowa ndikuyesedwa pa usiku wina kuchita chiwerewere. Ndidamtaya Mulungu ndipo ndinali ogalukira, monga bulu wa mtchire kuchita zanga zokha.

Ndikaona m'mbuyo, ndinkadziwa kuchokera pansu pa mtima kuti ndinkasowa mwamuna! Madzulo a tsiku lina, ndidayitanidwa ku phwando lalikulu la Khisimisi ndipo mwamuna wachikuda adandiyitana kuti ndipite naye limodzi kuphwandoko. Komatu munthuyu anali ndi zolinga zoipa ndipo adandigwililira mu chipinda cha ku Hotelo. Adali ataledzera ndithu ndikundikakamiza kuti ndigonane naye, kundikankhira ku khoma. Pambuyo pake, ndinadikira kuti atulukemo mu Hoteloyo ndipo ndidathawa ndikubwerera ku nyumba. Zinali zochititsa mantha.

Tsopano ndikaona m'mbuyo, ndimayamika Mulungu kuti ndikadali ndi moyo chifukwa zikadafika poyipa zedi. Ndinali ndili ndi zaka 25 choncho ndidachita mantha kuti ndiulule zimenezi ku polisi koma mzanga adandilangiza kuti ndikakumane ndi dotolo wa ku Univesite, ndipo ndidaterodi. Ndidamwa mankhwala kuti a dotolo ondiyesa thupi langa akaone kuti zonse zilibwino. Pambuyo pake pa kugwiriridwaku, ndinaonongedwa kwambiri ndipo zidandivuta kuti ndikhulupilire amuna.

Patapita nthawi, ndidaganiza zokhala ku England kuti ndimalize digiriyi yanga ndipo mchaka cha 2006 ndidakumana ndi mwamuna wabwino. Tsopano ameneyu ndiye mwamuna wanga, dzina lake ndi Daniele.

Tidakwatirana mchaka cha 2008 pa hotelo yokongola kwambiri ku UK, ndiyamika Mulungu chifukwa ndi mwamuna wabwino wa Chizungu. Mwachisoni, ndinadwala matenda a mu bongo mchaka cha 2010 ndikutengeredwa ku chipatala pa ambulansi. Ndidayezedwa ndi kupezeka ndi kachirombo ka HIV. Izi zinali zotsatira zakugwiriridwa kuja ndipo ndingafotokozere mokhudzika pakuti izi zinabweretsa bomba la likulu pa moyo wanga. Kufikira pano ndikukumbukira bwino mmene ndinachitira podziwa kuti ndili ndi kachirombo ka HIV ndidatenga mankhwala onse kuika pamaso panga

kuti ndimalize moyo wanga! Nyengo yanga inali yovuta kwambiri; madotolo adandiuza kuti ndinali pafupi kumwalira ndithu. Mwamuna wanga ankangosisima munjira ya mu holo ndipo iye adapezekanso ndi kachirombo ka HIV atayezedwa sabata yomweyo. Zinali zokhudza kwambiri ndi kuvulaza mwamuna wanga, amene ankagniza kuti mkazi wake akumwalira ndithu. Ndinali wokomoka kwa masiku atatu.

Pamene ndinkayezedwa HIV ndinali nditafulatira Mulungu. Mwadzidzidzi ndidakumbukira, “Ndine Mkhristu ndipo ndikhoza KUPEMPERA!” Choncho ndidayamba kupempha Mulungu kuti andilole ndikhale ndi moyo ndipo mwamuna wanganso anali ngati mngelo kundipempha kuti ndikhale ndi moyo! Kukhala kwanga mu m’bindikiro wa ku Chipatala kwa miyezi isanu ndi umodzi, inali nthawi ya mdima pa moyo wanga koma pomalizira pake ndidapita kunyumba. Tsiku lina, ndidamva luwu lomveka bwino kuti, “KoHsin bwerera kwa Ine. KoHsin bwerera ku Mpingo. Ndilikukuyembekezera”. Ndikukumbikira kuti panalibe munthu aliyense pa balaza, ndidadziwa kuti linali liwu la Mulungu choncho ndinatenga galimoto yolipira kupita ku mpingo ngakhale thupi langa linali lofooka. Kubzyolera mwa mankhwala, chisamaliro, upangiri wa Chikhristu ndi mapemphero a abwenzi a mu mpingo ndidakhalanso ndi moyo.

Phunziro loyamba lomwe ndidaphunzira ku mpingo ndilo kukhululukira mzimbambo yemwe adandigwilirira uja, kenako kudzikhululukiranso ndekha. Zinali zovuta kuti ndizichite komabe ndidachita mwa mphamvu ya Yesu Khristu. Ndidabvomereza tchimo langa ndi kukhululukira mzibamboyo komanso ndidadzikhululukira ndekha chifukwa chokapezeka kumaloko. Ndidapeza kumasuka kwambiri kuchokera kwa Ambuye ndipo tsopano ndikamaona m’mbuyo ndimadziwa kuti kugwiriridwako kudachitika koma ndidapeza machiritso ochuluka kuchokera kwa Ambuye.

Ndikadafa pa usiku womwe ndidagwiliridwa ku hoteloko. Ndikadafa pamene ndidayezedwa ndi kupezeka ndi HIV koma sindidafe mwa chisomo cha Mulungu! Pa nthawi yomwe ndidafulatira Ambuye kwathunthu ndipo ndinali uja mumatchula kuti Nkhosa Yosokera. Tsopano ndikudziwa kuti Mulungu amandikonda, adandiyitana kubwerera monga Mwana Wolowerera ndipo ndikacheukira kale langa ndithudi chitetezo cha Mulungu chinalipo!

Chifukwa choti ndinali ndi kachirombo ka HIV, kwa zaka zingapo ndidadziuza ndekha komanso mwamuna wanga kuti SINDIKUFUNA kukhala ndi mwana. Ine ndi mwamuna wanga tinali ndi HIV ndipo tinalibe bvuto kukhala zaka kufikira mwamuna wanga adandiuza molimba kuti akhale ndi banja ndipo anadalira chisamaliro cha chipatala ku UK. Ndidabvutika kwambiri ndi ganizoli ndiye ndidapita ku Taiwan kuti ndikaganizire ndi kupemphera! Mulungu

adanditengera ku ulendo wa utumwi wa gulu la Amayi a Chikhristu la Aglow ndipo paulendowu anzanga ambiri adandipempherera kuti ndichotse mantha ndi kupempha Ambuye andipatse chizindikiro ndi chitsimikiziro.

Chozizwa choyamba chinali pamene ndidatenga makhwala oyeserera ndipo mu nthawi yochepa kwambiri mulingo wa HIV udatsikiratu kuchoka pa 22,000 kufika pa ziro pa tsiku la 36 la kubadwa kwanga! Odziwa za HIV sadakhulupilire zomwe ankaona ndipo adandiuza kuti ngati ndikufuna kuyesera kukhala ndi mwana, iyi ndiyo nthawi yoyenera. Ndidazindikira kuti ichi ndi chizindikiro chochokera kwa Mulungu. Kenako kuyambira mu Julayi ndidayamba kuyesera kukhala ndi mwana ndipo mu Okutobala ndidapita ku chimsonkhano chachikulu chadziko lonse cha Chikhristu ku UK. Kunali amayi ochuluka kumeneko ndipo adandipempherera mu chipinda cha hotelo ku msonkhanowo ndipo mzimayi wina adalengeza kuti waona masomphenya kuti ndikhala ndi mwana wamkazi. Adandipempherera mwamphamvu kuti Mulungu atsekule mimba yanga kuti ndikhale woyembekezera mwana! Ndidatenga mimba mu Disembala ndipo mwana adabadwa pa 11 Ogasiti mwa kuchekedwa!

Mimbayi inali yobvuta kwambiri koma ndikaona m'mbuyo ndinkadziwa kuti inali yodzala ndi chisomo. Ndidaidikwa mu gulu la akatswiri a malangizo. Ndikukumbukira kuti tsiku lililonse ndimasanjika dzanja pa nchombo wanga kupempherera mwanayo ndi kumuyimbira nyimbo. Ndinadziwa kuti mwanayu ankamvetsera mawu anga mkatimo. Tsiku lomwe mwana adabadwa, Mulungu adandiuza kuti ndimutche dzina loti Hana kutanthauza "Wamtengo wapatali". Iye ndi chozizwa chachikulu zedi chifukwa alibe HIV. Hana ndi chozizwa ndipo adayezedwa nthawi zambiri ku UK ndipo nthawi zonse zotsatira zake zinali zoti alibe, Ambuye alemekezeke!

Zikomo Yesu! Ndikachewukira m'mbuyo pa Iye, sadanditaye mkomwe ndipo pamene ndidalephera kwa Mulungu, Iye sadalephere kwa ine. Pamene ndinali kufa ndi kachirobo ka HIV m'thupi langa lonse, Mulungu adapulumutsa moyo wanga. Chisomo chake mchokwanira ndipo kwa zaka khumi ndinadutsa mu ulendo wa machiritso. Tsopano ndidziwa kuti Mulungu akuyembekezera zabwino kwa ife ndipo Iye ndi Atate wathu wa Kumwamba. Timakhumudwa ndi anthu chifukwa anthu akhozadi kutikhumudwitsa, koma Mulungu ndi wokhulupirika ndipo sadzatikhumudwitsa mkomwe!

Moyo wanga udasinthika kwathunthu mwa mphamvu ya machiritso ndipo Mulungu adandiuza pa usiku wina pamene ndimkapempherera kuti ndipite kukachitira umboni wa dzina lake kwa mafuko onse motero ndakhala ndikuchita zimenezi. Ndikupereka ulemelero wonse kwa Ambuye Mulungu ndi kugwiritsa ntchito umboni wanga kufikira anthu ambiri pa dziko lonseli.

Pemphero langa tsopano ndilo kuti ubwerere kwa Yesu ndikuyamba kumukhulupirira. Zoonadi, Chiyembekezo chokhacho ndiye Yesu Khristu.

Nena pemphero ili la chipulumutso ndikulola Mulungu alowe mmoyo wako.

### **Pemphero la Munthu Wochimwa**

Atate wa Kumwamba, ndikubwera kwa Inu kuti mundikhululukire machimo anga. Ndikubvomereza ndi pakamwa panga ndi kukhulupirira ndi mtima wanga kuti Yesu ndiye Mwana wanu, ndipo adafa pa mtanda wa Karivari kuti ndikhululukidwe ndikukhala ndi moyo wosatha mu Ufumu wa Kumwamba. Atate, ndikukhulupirira kuti Yesu adauka kwa akufa ndipo ndikupempha tsopano kuti bwerani mmoyo wanga ndikukhala Ambuye ndi Mpulumutsi wanga. Ndikulapa tchimo langa ndipo ndidzakulambirani masiku onse a moyo wanga chifukwa mawu anu ndi choonadi. Ndikubvomereza ndi pakamwa panga kuti ndine wobadwanso mwatsopano ndiwosambitsidwa ndi mwazi wa Yesu! Mdzina la Yesu, Amen.

**HEALED IN VICTORY MINISTRY INTERNATIONAL**

Director: KoHsin Illingworth

Email: [kohsinillingworth@hotmail.com](mailto:kohsinillingworth@hotmail.com)

Web: [www.healedinvictory.org](http://www.healedinvictory.org)

Pastor Chikuta  
+265 999 627 114